



MUTU 13:

KU DZIKO LONSE
LAPANSI


CHIFUKWA CHOOPA
KUPHEDWA, AKHRISTU
ANKAKUMANA M'MALO
OBISIKA KUTI AMVE MALI
A MULLINGU NDI
KUMAYIMBA NYIMBO
ZOTAMANDA MULLINGU.

OKONDEDWA,
AMBUYE ATHU
ANAMVA ZOWAWA KUTI
ATICHOTSERE MACHIMO
ATHU. SICHACHILENDO
TSONO KUTI NAFENSO
TIKUVUTIKA CHIFUKWA
CHA IYE. MUSADABWE
TSONO CHIFUKWA
CHA MAZUNZO AMENE
TIKUKUMANA
NAWOWA.






YESU ANATI, "WINA
AKAFUNA KUKHALA WOPHUNZIRA
WANGA, MUNTHUYO AYENERA KUSENZA
MTANDA WAKE NKUMANDITSATA"
TSONO NDIYE KUTI TIYENERA KUSENZA
MITANDA YATHU MPAKA PA PHIRI
LIMENE AMAKHOMERAPO ANTHU NGATI
TAITANIDWADI KUKHALA OPHUNZIRA A
YESU. PAJA MASALIMO 22
AMATIENZA KUTI...



MULLINGU
TITHANDIZENI.
NDI CHIGAWENGA
CHIJA, **SALLO**.

KHALANI POMPO,
MUSATHAWE! CHIPEMBEDZO
CHACHILENDOCHI SICHOLELLEDWA.
MUMANYOZA MAKOLO NDI DZIKO
LATHU LOMWE. NDINU OPUZA!
MUYENERA KUSIYA KUTSATIRA
CHIPEMBEDZO CHIMENECHI,
APO AI, MUPHEDWA.

GWIRANI
MTSOGOLERI
WAOYO. AONERA
IYEYU. APHUNZIRAPO
PA ZIMENE TIMCHITE
MTSOGOLERIYO.



TAKHALAPO NDI
AMESIYA ODZIWIKA BWINO
AMBIRIMBIRI. NCHIFUKWA
CHIYANI MUKUPEMBEDZA
KALIPENTALA WAKUFA?

AMBUYE ATHU
YESU NDI WAMOYO
NDIPO NDI MLENGI WA
DZIKO LAPANSI NDI
KUMWAMBA.

TIKAPONYA
MKAZI WAKO
M'NDENDE NDI PAMENE
USINTHE MAGANIZO,
NKULEKA ZIMENE
UKUKHULLUPIRIRAZO.




MATEYU 16:24; MACHITIDWE 9:1-2



LIYUNSO
NDI MMODZI MWA
ANTHU OKONDA
KHRISTU.

NTHAWI
IMENE TINAKHALA
AKHRISTU TINADZIWA
KUTI ZIMENEZI
ZIDZATICHITIKIRA.



INDE,
TIYENERA
KUMPEMPHERERA.
TIPEMPHERE KUTI
MULLINGU AFEWETSE
MTIMA WAKE NDIPO
KUTI AMUONETSE
CHOONADI.

NDI M FARISI UJA
WOTCHEDWA SAULO.
AKUDANA NDI AKHRISTU,
NCHIFUKWA CHAKE
WAPHA AMBIRI.

KUMBUKIRANI,
ENA A IFE TINALI
OKAIKA PAMENE
TINKAYAMBA
CHIKHRISTU.

SAULO
NDI MUNTHU
WANKHANZA
KWAMBIRI.



SALULO, NDIKUGANIZA
KUTI AMBIRI OTSATIRA
MPATUKO WA YESU MUNO
MU YERUSALEMU WATHANA
NAWO NDITHU.

SICHONCHO,
MMENE ZIKUCHITIKIRA NKUTI
TIKAMANGA AKHRISTU AMBIRI NDI
KUWAPONYA M'NDENDE, NDI PAMENE
AKUCHULLUKIRACHULLUKIRA. AMWAZIKIRA
M'MIZINDA INA. M'MASUNAGOGE
AMBIRI KU DAMASIKO MULI
AKHRISTU AMBIRI.



NDIKUPATSA
CHIOLEZO CHOTI
LIZIWAMANGA,
NDIPO LIPITE KU
DAMASIKO.

NDIPITA
POMPANOPOMPANO.

SAULO AMAGANIZA KUTI UDINDO WAKE
UNALI WOTETEZA CHIPEMBEDZO NDI
DZIKO LAKE KWA ANTHU A ZIPEMBEDZO
ZINA. KOMA ANKADABWA POONA KUTI
AKHRISTU AMAONEKA AMTENDERE
KOMANSO OLIMBA MTIMA.




POSAKHALITSA KUWALA KOPOSA
DZUWA KUNAMUONEKERA SAULO.

A man with a beard and long hair, wearing a dark tunic and a purple sash, is riding a brown horse. He has a look of intense distress or anger, with his hands raised to his face. The horse is also depicted with a sense of motion and strain. The background is filled with dynamic, radiating lines, suggesting a chaotic or high-stakes situation. A jagged, yellow speech bubble is superimposed over the scene, containing the text 'SAULO, SAULO, UKUNDIZUNZIRANJI?'.

**SAULO, SAULO,
UKUNDIZUNZIRANJI?**

KAVALO WA SAULO ANACHITA
MANTHA KWAMBIRI NDIPO
ANAMGWETSA PANSI MU
MSEU, KAVALOYO NKUTHAWA.



NDINU YANI,
AMBUYE, KUTI INE
NDIKUKUZUNZANI?

INE NDINE YESU,
AMENE UKUNDIZUNZA
UKAMALANGA ANTHU
AMENE
AMANDITSATIRA.

NYAMUKA. PITA
MU MZINDA, NDIPO
KUMENECO UKAUZIDWA
CHOTI UCHITE.

AMBUYE,
MUFUNA KUTI
NDITANI?

MACHITIDWE 9:3-6




KODI
MUNAMVA
MALI?

INENSOTU
SINDINAMVETSE.
ANAMVEKA NGATI
BINGU.

INDE, KOMA
SINDINAMVETSE
ZOMWE MALIWO
AMANENA.

SINDIKUONA!
THANDIZENI.
SINDIKUONA.
PITANANENI
MUMZINDAMO.

**NDI MALI A
MULLINGU!**



INE NDINE ANANIYA.
YESU ANAYANKHULA NANE
M'MASOMPHENYA. ANANDIENZA
KUTI NDIBWERE KWA IWE NDIPO
IYEYO AKUPENYETSANSO.


ZOONADI
NDINE
WAKHUNGU.

M'DZINA LA
YESU KHRISTU,
PENYANSO.



**NDIKUONA!
MUKUTI WACHITA
ZIMENEZI NDI YESU?
UZENI ZAMBIRI ZA
YESU AMENEYU.**






CHONCHO ANANIYA ANATSEKULA
MALEMBO, NAONETSA SAULO
UNENERI WOKHUDZA YESU.

INDE, NDAKHALA
WOPUSA NTHAWI YONSEYI.
ZONSEZI ZILI M'MALEMBO NDITHU.
NDINALI WAKHUNGU CHIFUKWA
CHOKONDA CHIPEMBEDZO CHANGA.
NDIKUFUNA MUNDIBATIZE KUTI
NDIKHALE WOTSATIRA YESU.

MULLINGU ANASINTHA
DZINA LA SAULO NDI
KUKHALA PALLO.

MACHITIDWE 9:7-19



SALUO, WOTCHEDWA PAULO
TSOPANO, ANAKHALA MUNTHU
WATSOPANO, WA UTHENGANSO
WATSOPANO. SANAFUNENSO
KUMAPHA AKHRISTU. ANAFUNA
KUUZA ENA KUTI AKHULUPIRIRE
YESU KHRISTU.


NDIKUMVETSA
CHIFUKWA CHOMWE
MUKUKAIKIRA. INENSOTU
SINDINKAKHULUPIRIRA.
KOMATU NDIKUKUUZANI
KUTI YESU WA KU NAZARETE
ANAKWANIRITSA ZONSE
ZIMENE ANENERI ONSE
ADANENA ZOKHUDZA
MESIYA WATHU.

KANI NDIWE
WOPUSA CHONCHI?
MESIYA AKANALOLERA
BWANJI KUTI APHEDWE
NDI ADANI ATHU?



ANALI
MWANAWANKHOSA WA
MULLINGU KUTI ACHOTSE
MACHIMO ATHU.

KOMA
CHIZINDIKIRO
CHACHIKULU NKUTI
MULLINGU
ANAMUUKITSA
KWA AKUFA.




MULLINGU ANKAGWIRANSO
NTCHITO NDI ANTHU
A MITUNDU INA.
PANALI MSILIKALI WINA
WACHIROMA AMENE
ANKAFUNAFUNA MULLINGU
M'MAPEMPHERO AKE.

MULLINGU, NDIKUDZIWA
KUTI NDINU NOKHA BASI, MLENGI
WA ANTHU ONSE. CHIPEMBEDZO CHA
ANTHU A MTUNDU WANGA NCHOIPA
NDIPO SICHIPEREKA MTENDERE.
ONETSENI NJIRA YANU NDIPO
NDIDZAYENDA M'MENEMO.



NDANI?
CHIYANI?
NDINU YANI?
MWACHOKERA
KUTI?

MAPEMPHERO AKO
AMVEKA. MULLINGU WANDITUMA.
UTUME ANTHU APITE KU **YOPA**,
KUNYUMBA KWA **SIMONI** MMISIRI WA
ZIKOPA. NYUMBAYO ILI M'MPHEPETE
MWA NJANJA. KUMENEKO AKAFUNSE
ZA MUNTHU WINA WOTCHEDWA
PETRO. ADZABWERA KUNO NDIPO
ADZAKUUZA ZOONA ZENIZENI
ZA MULLINGU.



MULLINGU
WABWERETSA
MTENDERE
KUDZERA M'MWAZI
WOKHETSEDWA
PA MTANDA.

PETRO, BWANA WATHU
NDI MUNTHU WOPEMBEDZA KWAMBIRI,
MUNTHU WABWINO, KOMA AMAVUTIKA NDI
ZINTHU ZAMBIRI. AMAPEMPHERA NTHAWI
ZONSE NDIPO AMAPEREKA NDALAMA KWA
ANTHU OSAUKA, KOMA ALIBE MTENDERE
WOCHOKERA KWA MULLINGU.

ZIMENEZI
ZIKUTANTHAUZA
CHIYANI?

NDIKALONGOSOLA
ZIMENEZI KWA
BWANA WANU.



MKULU WA ASILIKALI UJA
AKUKUMANA NDI PETRO
NKUGWADIRA PETROYO.


DZUKANI.
MUSAPEMBEDZE INE.
INE NDINE MUNTHU MONGA
MOMWE MULILI INUYO. ITANANI
ANTHU ONSE KUTI NDIKUUZENI
LTHENGA WABWINO.

MACHITIDWE 9:20-22,
10:1-27, 38-41

LERO NDI TSIKU LALIKULU.
MULINGU WATUMA PETRO,
MMODZI MWA OPHUNZIRA A YESU,
KUTI ADZATIENZE ZA YESUYO.

INDE, NDINAKHALA NDI YESU KWA
ZAKA ZITATU NDI THEKA. NDINAMUONA
AKUKHOMEDWA PA MTANDA, NDIPO NDINAMUONANSO
ATAUKA KWA AKUFA. TIDALIPO ANTHU 500 AMENE
TIDASONKHANA PA MALO AMODZI KUTI TIMVE ZIMENE
YESU ADAFUNA KUTILALIKIRA ATAUKA KWA AKUFA.
ADADYA NAFE NDIPO TIDAMUKHUDZA. ANATIPHUNZITSA
KUTI TIZIKONDA ADANI ATHU NDI KUMAPEMPHERERA
AMENE AMATIZUNZA. ADATUMIZA
MZIMU WAKE...

KAPUTENI KONERIYO
NDI ONSE A PA BANJA LAKE
ANAKHULUPIRIRA LITHENGA
WA YESU KHRISTU NDIPO
ANABATZIKA TSIKU LIMENELO.






MUMANDIDZIWA.
NDINKAZUNZA AKHRISTU MPAKA
KUMAWAPHA KUMENE, KOMA YESU
ANANDIONEKERA M'KUWALA KOCHITITSA
KHUNGU, NDIPO NDI MAU NGATI BINGU
ANANDIENZA KUTI NDIZILALIKA MAU AKE.
NDAFUFUZA M'MALEMBO ZOKHUDZA
MESIYA NDIPO NDAPEZA KUTI YESU
ANAKWANIRITSA UNENERI
WONSE.

PAULO ANALOWA M'SUNAGOGE
PA TSIKU LA SABATA KU ANTIOKO
NDIPO ANALALIKA LITHENGA
WABWINO KWA AYUDA.






MULLINGU ADATI
ADZAUTSA MWANA WA DAVIDE
KUTI AKHALE MESIYA WA ISRAELE,
NDIPO KUTI ATSOGOLERI A KU
YERUSALEMU ADZAMUKANA
MPAKA ADZAPHEDWA.

M'MASALIMO
2 MWALEMBEDWA
KUTI, "NDIWE MWANA
WANGA, LERO LINO
NDAKUBALA."

M'MASALIMO ENA AKUTI
MULLINGU SADZALOLA KUTI
WOYERA WAKE AVUNDE. UMENEWU
NDI UNENERI WAKUTI, NGAKHALE
ADZAMWALIRA, THUPI LAKE
SILIDZAONONGEKA. DZIWANI LERO
KUTI MWA YESU NDIMO MMENE
MUNGAPEZEMO CHIKHULULUKIRO
CHONSE CHA MACHIMO ANU
CHIMENE MOSE SANATHE
KUPEREKA.





MULLINGU
ADATUMA YESU
KUTI AKHALE MUUNI
KWA **ANTHU A MITUNDU
INA**, MPULUMUTSI
WA MAIKO ONSE.

**ANTHU A
MITUNDU INA!**
ANTHU A MITUNDU
INA NDI ODETSEDWA.
CHIKHULLUPIRIRO CHAO
SICHINGAFANANE
NDI AYUDA.


UKUNYOZA MULLINGU!
YESU SANALI MWANA WOBADWA
MOLONGOSOKA. AKUTI AMAI
AKE ANALI NDI PAKATI
ASANAKWATIWE.

MASLIMO 2:7,
16:10; MACHITIDWE
2:27, 10:47, 13:35



UKHOZA
KUPHEDWA NDI
MIYALA CHIFLUKWA
CHA BODZA
LAKOLO.

POPEZA MWAKANA
LITHENGA WABWINO
WOPATSA MOYO WOSATHA, IFE
TIPITA KUKALALIKIRA ANTHU A
MITUNDU INA, MONGA MOMWE
ANENERI ADANENERA.



PAULO ATADZIWA
KUTI MTUNDU
WA AYUDA
UZIKANABE KHRISTU,
ANALIMBIKA
ZOGWIRA NTCHITO
PAKATI PA ANTHU
A MITUNDU INA,
ANTHU AMENE
SANALI AYUDA.

ALEMEKEZEKE
MULLINGU NDI MWANA
WAKE YESU. CHIPULUMUTSO
CHAFIKIRA **ANTHU A
MITUNDU INA!**

**PAULO,
BATIZE!**

TIUZENI
ZAMBIRI
ZA UNENERI
WOKHUDZA
YESU.

ANTHU AMBIRI A MITUNDU
INA ANAKHULLUPIRIRA
LITHENGA WABWINO
NDIPO ANAPITIRIRA KUKHALA
M'CHISOMO CHA MULLINGU.



AYUDA ANAKWIYA NDIPO ANAPIRIKITSA
PAULO NDI BARNABASI MU MZINDAWO.
ANAWAOPSEZA KUTI ADZAWAPHA
AKADZABWERANSO. CHONCHO PAULO
NDI BARNABASI ANAPITA KU ASIYA NDIPO
ANALALIKA UTHENGA WABWINO KWA
ALIYENSE AMENE ANKAKUMANA NAYE.


BARNABASI,
INE NDIKAGWA,
IWEYO UZITHAWABE.
USAIME.

KU LUSTARA, AYUDA
ANAMPONYA MIYALA PAULO
MPAKA PAULOYO ANALI
PAFUPI KUFA, NDIPO
ANAPONYA THUPI LAKE
KUNJA KWA MZINDA.



AMBUYE
MUWAKHULULUKIRE.
APHA PAULO.


MACHITIDWE 14:18-19



KOMA MULLINGU
ANACHITA CHOZIZWA
NDIPO ANAMUUTSA
PAULO UJA.

PAULO,
NDIMAGANIZA
KUTI *WAF!*

AI, NKADALI MOYO.
MULLINGU ANANDIONETSA ZINTHU
ZAMBIRI KUTI NDIDZAZUNZIKA CHIFUKWA CHA
DZINA LAKE, NDIPO ICHI NCHIYAMBI CHABE.
TIYE TIBWERERE MUMZINDAMO.



MWAYENERA,
AMBUYE,
KULANDIRA
ULEMERERO,
ULEMU NDI
MATAMANDO...

KU FILIPI WA KU MASEDONIYA, PAULO
NDI SILA ANAKWAPULIDWA MIKWAPULO
39, KENAKA NKUWATSEKERA M'NDENDE.
POSALABADIRA MASAUTSO AO, MITIMA
YAO INADZAZA NDI CHIMWEMWE, NDIPO
PAKATI PA USIKU ANAYAMBA KUYIMBA
NYIMBO ZOTAMANDA MULLINGU.





AAAAAA!
YESU NDI
AMBLIYE!



HWAPU!

PAULO ANAMENYEDWAPO
KATATU NDI NDODO PA
ZAKA ZINA ZITATU. KOMABE
SANASIYE KULALIKA YESU.

MACHITIDWE 14:20, 16:23-25; 2
AKORINTO 11:24-25; CHIVUMBULITSO 4:11

PAMENE PAULO ANKAYENDA MALO
OSIYANASIYANA KULALIKA UTHENGA
WABWINO, SITIMA ZAPAMADZI
ZIMENE ANKAKWERA ZINAMIRAPO
M'MADZI KATATU KONSE.

PAULO ANKAKUMANA
NDI ANTHU AMBANDA
KAWIRIKAWIRI.



TSIKU LINA ANAKHALA
M'NYANJA TSIKU LONSE
POLINDIRA KUTI SITIMA
INA IMUTOLE.




KOMA SANASIYE
KULALIKA.

PAULO ANKAVUTIKA NDI
MATENDA, KUZIZIRA, KUTENTHA,
NJALA, NDI ZOSAUTSA ZINA
ZAMBIRI, PAMENE ANKAYENDA
M'MADERA OSIYANASIYANA
KUUZA ANTHU ZA YESU.



AMBUYE,
CHIRITSANI THUPI
LANGALI KUTI NDI THE
KUPITA KUKALALIKA
MU MZINDA WINA.

PAULO ANAPITA M'MIZINDA YOSIYANASIYANA
KUCHENJEZA ANTHU ZA KUPEMBEDZA MAFANO NDI
KUMAWAUZA ZA UTHENGA WABWINO WA YESU KHRISTU.



MWATEMBENUKIRA
KWA MULLINGU NDIPO
MWASIYA MAFANO ANU.
MULLINGU WAKULUNGAMITSANI
CHIFUKWA CHA CHIKHULUPIRIRO
CHANU, OSATI CHIFUKWA CHA
LAMULO LINA LILILONSE. TSOPANO
NDINU CHIHALO CHA THUPI LAKE,
NDIPO NDINU A M'BANJA
LA MULLINGU.

**MULLINGU
ALEMEKEZEKE!**

1 AKORINTO 10:14, 12:12-13, 18; 2 AKORINTO
11:25; AGALATIYA 2:6; AEFESO 2:19



ICHI
SICHINKANDIPATSA
MTENDERE.

PAMENE ANTHU ANKATEMBENUKIRA KWA MULLINGU, ANTHUWO ANKASIYA MAFANO NDI NYANGA ZAO. ANKATAYIRA PA MOTO MACHIMO AO NDI ZONSE ZOKHUDZANA NDI CHIPEMBEDZO CHAO CHAKALE. KWA ZAKA ZO CHABE, ANTHU AMBIRI M'MADERA OSIYANASIYANA ANAKHULLUPIRIRA LITHENGA WABWINO NKUMAPEMBEDZA MULLINGU KUDZERA MWA YESU KHRISTU.

YESU ADACHENJEZERATU OPHUNZIRA
AKE KUTI, "ADZAKUPEREKANI KUTI
AKUZUNZENI, NDIPO ADZAKUPHANI:
ANTHU ONSE ADZADANA NANU
CHIFUKWA CHA DZINA LANGA.
AMBIRI ADZAKHUMUDWA NANE
NDIPO ADZAPEREKA ANZAO KWA
ADANI, NDIPONSO ADZADANA
NDI ANZAOWO. ANENERI AMBIRI
ONYENGA ADZAONEKA, NDIPO
ADZANAMIZA ANTHU AMBIRI."



AMBUYE YESU,
LANDIRANI MZIMU
WANGA!



PAMENE ANTHU AMENE ADAONA YESU
ANALI KUKALAMBA, NTHAWI IMENE MPINGO
UDAFALA MU UFUMU WONSE WA AROMA,
AROMA ADAYAMBA KUFUNAFUNA AKHRISTU
NDI KUYAMBA KUWAZUNZA MWANKHANZA
MPAKA KUMAPHA ENA MWA IWO.
OKHULLUPIRIRA AKAPANDA KUKANA KHRISTU,
ANKAWAIKA M'BWALO LA ZAMASEWERO,
NDIPO ANTHU ANKAONENERA MIKANGO NDI
AKAMBUKU ZIKUWADYA OKHULLUPIRIRAWO.

ATATE, MUSAWALANGE
CHIFUKWA CHA ZIMENE
AKUTICHITIRAZI.

GIGIRIIII!



EEEE!


NTHAWI ZINA AKHRISTU ANKAPHEDWA
NDI ASILIKALI ACHIROMA. ANTHU
ANKADABWA POONA KUTI
OKHULUPIRIRAWO ANKAKANGAMIRABE
YESU. ANALI OKONZEKA KUFA
CHIFUKWA CHA YESUYO.



YASONI,
TIKAONANA KU
PARADIZO.

AAA!

MATEYU 24:9-11



YESU ASANAFE,
ADANENERATU
ZA TEMPILE:

KODI MUKUIONA
TEMPILEYI? NDIKUKUZANI
KUTI IDZAONONGEKA NDIPO
PALIBE MWALA UMENE
UDZAKHALA PA
UNZAKE.

ZAKA 40 PAMBUYO PA UNENERI
WA YESU UJA, M'CHAKA CHA
70 A.D., AROMA ANAONONGA
TEMPILE PAMODZI NDI MZINDA WA
YERUSALEMU. MATABWA ATAYAKA
M'KATI MWA TEMPILEYO, GOLIDE
WA MU TEMPILE ANASUNGUNUKA,
NKUMAYENDERERA M'MING'ALU
PAKATI PA MIYALA YAPANSI NDI
YAM'MAZIKO. PAMENE AROMA
ANAFUNA KUDZATENGA GOLIDE WA MU
TEMPILE UJA, ANAONA KUTI KUNALI
BWINO KUTI AGUMULE TEMPILEYO.
MALI A YESU ANAKWANIRITSIDWADI.

AYUDA A MU YERUSALEMU NDI A
KU ISRAELE AMENE ANAPULUMUKA
PA NKHONDOYO, ANATHAWIRA
M'MAIKO A ANTHU A MITUNDU
INA, KUMENE AMBIRI MWA ANA AO
AKUKHALA MPAKA LERO LINO.



TIPITA KUNYUMBA
KWA MLONGO WANGA
KU SIRIYA.

AKHRISTU ACHIYUDA NAWONSO
ANATHAWIRA M'MAIKO ENA
KUMENE ANKALALIKA LITHENGA
WABWINO WA KHRISTU, NDIPO
MPINGO UNAKULA.

KULIKONSE KUMENE
ANKAPITA KUNALI
KALE AKHRISTU, OMWE
ANKAWALANDIRA.



TINALIBE
KOLOWERA.

TAMVA ZOOPSA
ZIMENE ZACHITIKA
KU YERUSALEMU.
PALIBE CHOLETSA
KUTI MUZIKHALA
NAFE.

MATEYU 24:2; LUKA 19:43-44

PA MOYO WAO WONSE, ATUMWI A YESU ANAPITIRIRABE KULALIKA UTHENGA WAKUTI YESU KHRISTU ANAUKA KWA AKUFA. MMODZIMMODZI WA IWO ANAYAMBA KUPHEDWA. ONSEWO ANAFA MOLIMBA MTIMA, PODZIWA KUTI ANALI NDI MUDZI WABWINO KWAMBIRI KUMWAMBA.



ENA ANAKHOMEDWA PA MTANDA NDI AROMA.

ENA ANKATUMBULIDWA ALI MOYO KENAKA NKUMAWADULA NTHULINTHULI.



ENA
ANAPHEDWA
POWAPONYA
MIYALA.

ENA ANAPEREKEDWA KUTI
AKHALE CHAKUDYA CHA
NYAMA ZAKUTHENGO.

ENA ANADULIDWA MITU.

MATEYU 14:10; YOHANE 21:18

PETRO ANAKHOMEDWA
PA MTANDA MOZONDOKA.

ENA ANKAWAOTCHA
M'MAFUTA
PANG'ONOPANG'ONO.

NDIKUPITA
KU MALO ABWINO
KOPOSA. MULINGU
AKUKHULULUKIRENI.

INDE
SINDIYENERA
KUFA MONGA MMENE
INU MUDAFERA,
AMBUYE.

ONSE ANAFA AKUKHULUPIRIRABE KHRISTU, ALI
NDI CHITSIMIKIZO CHOTI MATUPI ATSOPANO
NDI MALO ABWINO KOPOSA AKUWALINDIRA.



PATATHA ZAKA GO YESU ATAUKA
KWA AKUFA, MWA ATUMWI A YESU,
YOHANE YEKHA NDIYE ANATSALA.
ANAMUIKA M'NDENDE PA CHILUMBA
CHAMIYALA CHOTCHEDWA
PATIMOSI. MZIMU ANAMUFIKIRA
YOHANE NAPITA NAYE KUMWAMBA
KOMWE ANAMUONETSA ZINTHU
ZAM'TSOGOLO.



**YOHANE,
NDIKUONETSA
ZINTHU ZIMENE ZIDZACHITIKA
M'TSOGOLO. LEMBA ZIMENE
UKUONA, UZISUNGIRE M'BUKU
NDIPO UZITUMIZE KU MIPINGO
ISANU NDI IWIRI YA
KU ASIYA.**



NTHAWI YAPANSIPANO
IKAKHALA PANG'ONO KUTHA, YESU
ADZABWERANSO NDIPO ADZATSEKULA
MANDA A ANTHU ONSE AMENE
AMAMUKHULLUPIRIRA. IWOWO, NDI
OKHULLUPIRIRA ENA ONSE AMENE
ADZAKHALA ASANAFE PA NTHAWIYO,
ADZATENGEDWA KUPITA KUKAKUMANA
NDI YESU MLENGALENGA NDIPO
ADZAKHALA NDI IYE MPAKA MUYAYA.



PA MASIKU OMALIZA, MULLINGU
ADZALANGA DZIKO LAPANSI NDI
ZOSALITSA ZOOPSA KWAMBIRI.
MOTO LDZATSIKA KUCHOKERA
KUMWAMBA NDIPO PADZAKHALA
MILIRI IMENE IDZAONONGA ANTHU
AMBIRI OKHALA PA DZIKO LAPANSI.

MUNTHU WINA ADZABWERA AMENE
AZIDZATI NDI MESIYA, NDIPO ADZANYENGA
ANTHU AMBIRI. ADZACHITITSA KUTI ANTHU
AZIMULEMEKEZA PAMODZI NDI BOMA LAKE.
CHONCHO ANTHUWO ADZALANDIRA
CHIZINDIKIRO PAMPHUMI KAPENA KUSERI
KWA MANJA AO AMANJA.

1 ATESALONIKA
4:14, 16-17; 2
ATESALONIKA 2:2-3;
CHIVUMBULITSO 1:9,
11, 8:1-13, 9:18, 13:16,
20:4



AMENE ADZAKANA KULANDIRA CHIZINDIKIROCHO
ADZAPHEDWA PODULIDWA ZIHALO PANG'OPANG'ONO.
IDZAKHALA NTHAWI YOWAWITSA KWAMBIRI KWA
ANTHU AMENE ADZATSALE PA DZIKO LAPANSI.

MONGA ZINALEMBEDWERA,
YESU ADZABWERANSO PAKUTHA
PA NTHAWI YAPANSIPANO.

ADZABWERA NDI
ULEMERERO NDI
MPHAMVU ZONSE;
OSATINSO
MONGA MUNTHU
NGATI IFE.
KUMWAMBA
KUDZATSEKUKA
NDIPO IYEYO
ADZATSIKA
ATAKWERA KAVALO
WOYERA.



ADZAWALA NGATI DZUWA NDIPO
ADZAVALA ZISOTI ZACHIFUMU
ZAMBIRIMBIRI PAMUTU PAKE.
ADZANYAMULA NYENYEZI ZISANU
NDI ZIWIRI M'MANJA MWAKE NDIPO
M'KAMWA MWAKE MUDZATULLUKA
LUPANGA LA CHOONADI.

ADZALIMBANA NDI SATANA NDIPO
ADZAMUPONYA M'NYANJA YA MOTO
KUMENE ADZAZUNZIKA MPAKA
KALEKALE, PAMENEPO SATANA
SADZAYESANSO ANTHU KUTI ACHIMWE.
YESU ADZAPONYANSO IMFA, MDANI
WAKE WOTSIRIZA, M'NYANJA YA
MOTO NDIPO DZIKO LAPANSI
ADZALIPANGA KUKHALA LATSOPANO.



MULLINGU ADZASONKHANITSA ANTHU
ONSE AMENE ADAKHULLUPIRIRA
MWANA WAKE NDI KUWAPATSA
MOYO WOSATHA M'DZIKO
LAPANSI LATSOPANOLO. MULLINGU
ADZAWAPUPUTA MISOZI YONSE
NDIPO SIKUDZAKHALANSO MALIRO,
CHISONI, KULIRA NDI ZOWAWA, PAKUTI
ZINTHU ZAKALE ZIDZAPITA. YESU,
MONGA MFUMU NDI MPULUMUTSI,
ADZALAMULA ANTHU AKE M'DZIKO
LOPANDA TCHIMO NDI IMFA.

1 ATESALONIKA 4:16; CHIVUMBULUTSO
1:16, 19:11-21, 20:10-15, 21:1-4



LITHEGA WABWINO
WA YESU KHRISTU
WALALIKIDWA KWA
ZAKA 2000. YESU
ADALOSA KUTI
LITHEGA WAKE
LIDZAFALIKIRA DZIKO
LONSE LAPANSI
MPAKA DZIKO
LILILONSE, MTUNDU
ULIWONSE, NDI
BANJA LILILONSE
LIDZAMVE LITHEGA
WAKE WABWINOWO.



MULUNGU NDI
MMODZI, NDIPO ALI
NDI MWANA MMODZI.
CHIKHULUPIRIRO
NDI CHIMODZI,
NDIPO BAIBULO
NDI LIMODZINSO.
PALI NJIRA
IMODZI YOLOWERA
KU PARADIZO
MOYO WATHUWU
UKADZATHA PANSI
PANO. YESU NDIYE
NJIRA, CHOONADI,
NDI MOYO, NDIPO
ANTHU AMBIRI PA
DZIKO LAPANSI
APEZA KUTI ZIMENEZI
NDI ZOONA.

LITHENGA WABWINO WONENA ZA YESU KHRISTU NDI WOSIYANA NDI ZIPEMBEDZO ZINA ZA PA DZIKO LAPANSI, CHIFUKWA LITHENGAWU SUFALA CHIFUKWA CHA NKHONDO KAPENA CHIFUKWA CHOOPSEZA ANTHU. YESU ANAPHUNZITSA OMUTSATIRA KUTI AZIKONDA ADANI AO NDI KUTINSO AZIKONDWA NDI KUMAYIMBIRA MULLINGU. LERO LINO, ANTHU AMBIRI A M'MAIKO ONSE PA DZIKO LAPANSI AKUKONDWA CHIFUKWA CHAKUTI MULLINGU ADAWAKHULLULLUKIRA MACHIMO AO NDI KUTINSO ALI NDI MOYO WOSATHA.



KOMABE, PAPITA ZAKA PAFUPIFUPI 2000 KUCHOKERA PAMENE YESU ADAUKA KWA AKUFA, NDIPO PALI ENA AMENE SADAMVEPO LITHENGA WABWINO. PAFUNIKA KUTI WINA AWALIZE.

YOHANE 3:16, 14:6

Our desire is that after reading *Good and Evil*® you will be motivated to read the entire Bible and that it will come alive to you. Make it a daily habit to read a portion of the Bible and then pray that God will help you understand and apply it.

Copyright © 2008, 2017
Michael and Debi Pearl.
ALL RIGHTS RESERVED.

Author: Michael Pearl

Artist: Danny Bulanadi

Coloration: Clint Cearley



<https://goodandevilbook.com/>